# Kuchoka Ku Kuchita Bwino pa Chuma kufikira ku Khazikika

## NDONDOMEKO YA ZACHUMA YOKOMERA ANTHU 2024/25




Dziwani zambiri:

**Mlembi wamkulu wa mu unduna wa za chuma**

PO Box 30049, Lilongwe, Malawi
Imbani: +265 1 789 355
Imelo: budget@finance.gov.mw

**www.finance.gov.mw**



Ndi thandizo lochokera ndi European Union, Boma la Ireland ndi UNICEF.

Rialtas na hÉireann
Government of Ireland

unicef for every child


### CHUMA CHA DZIKO LA MALAWI

Chuma cha dziko la Malawi chidatsika mphamvu kuchoka pa 1.9 pa 100 iliyonse (kapena kuti peresenti) kufika pa 1.5 peresenti mchaka cha 2023. Izi zidachitika chonchi pazifuka zingapo monga kusowa kwa ndalama zakunja zomwe zidapangitsa kuti dziko lisagule mokwanira katundu monga feteleza ndi mafuta a galimoto. Kuona chitsogolo, chuma chikuyembekezereka kukwera ndi 3.2 peresenti mu chaka cha 2024 komanso 4.8 peresenti mu 2025. Izi ndi Kamba chiyembezeko kuti dziko lino likolola zochuluka kuchokera ku minda yikuluyikulu (megafamu) komanso kuchuluka kwa phindu lochokera ku zomangamanga ndi ku makampani wopanga katundu mwa zina mwa izo.

Mitengo ya katundu idakwera kuchoka pa 20.9 peresenti mu 2022 kufika pa 28.8 peresenti mu 2023. Koma pali chiyembekezo choti mitengoyi idzitsika pang'onopang'ono kufika mpakana 27.1 peresenti mu 2024 ndikudzatsikanso kwambiri kufika pa 12.4 peresenti mu 2025. Izi zidzatheka chifukwa cha zokolola zochuluka zomwe dziko lino likuyembekeza kupeza komanso potengera kuchepa kwa zotsamwitsa pa chuma zomwe zinagwera dziko lino posachedwapa.

### MMENE NDONDOMEKO YA CHUMA YA MCHAKA CHA 2024-25 YAKONZEDWERA

Ndondomeko ya zachuma ya mchaka cha 2024/25 ndi yokulirapo ndi 38.6 peresenti kulekana ndi ndondomeko ya mchaka cha 2024/24. Yachoka pa K4,329.1 biliyoni mu mchaka cha 2023/24 kufika pa K5,998.8 biliyoni mu 2024/25. Izi zili chomwechi kaamba koti boma likufuna kubweza ngongole zamgonagona mu 2024/25, kufunikira kowonjezera ndalama ku ntchito zaumoyo, za ulimi, ndi maphunziro, komanso ntchito zina zokonzekera zisankho za panayi zomwe zidzachitike mchaka cha 2025.

**Kuchuluka kwa chuma chomwe Boma litolere ndi Kulandira**
Pali chiyerekezo choti mchaka cha chuma cha 2023-24, kuchuluka kwa ndalama zomwe boma litolere komanso kulandira kuchokera ku mayiko ndi mabungwe omwe amalithandiza dziko lino zifika pa K4,329.1 biliyoni (yomwe ndi 24.3 peresenti ya chuma cha dziko lino). Mwandalamazi, K3,383.8 biliyoni yitoleredwa mdziko mommuno komanso K1,1683.8 biliyoni yidzachokera ku mayiko ndi mabungwe omwe amathandiza dziko lino. Pa ndalama yolinganiziridwayi, pali chiyembekezo choti ndalama zamisonkho zikwana K3,257.3 biliyoni yomwe ikuyimira 71.5 peresenti; tikuyembekezanso kutolera kunjira zina ndalama zokwana K126.5 biliyoni, yomwe ikuyimira 4.5 peresenti; ndipo tikuyembekezera kuti mabungwe ndi mayiko omwe amatithandiza atipatsa ndalama zokwana K1,168.4 biliyoni, yomwe ikuyimira 25.6 peresenti.

Mchaka cha chuma cha 2024/25, pali chiyembekezo chakuti boma litolera ndalama zokwana K3,257.3 biliyoni kudzera mmisonkho zomwe ndi zochulukirapo ndi 32.5 peresenti kuyerekeza ndi K2,198.1 biliyoni yomwe idatoleredwa mchaka cha zachuma cha 2023/24. Palinso chiyembekezo choti boma litolera ndalama zochulukirapo ndi 9.6 peresenti kufika pa K126.5 biliyoni kuchoka pa K114.3 biliyoni yomwe idatoleredwa mchaka cha zachuma cha 2023/24. Izi ndi kaamba ka kukhazikika kwa mphamvu za magetsi ndi mafuta a galimoto komanso ntchito zomangamanga.


Pa ndalama zokwana K1,168.4 billiyoni zomwe tikuyembekezera kuti tilandira kuchokera kwa mabungwe ndi mayiko omwe amatithandiza, K72,7 biliyoni idzachokera ku mayiko monga Norway ndi Germany pamene K1,095.7 biliyoni idzachokere ku mabungwe monga World Bank, African Development Bank, International Fund for Agricultural Development (IFAD), Flanders komanso Global Environmental Facility.

Polinganiza ndi chaka cha chuma cha 2023/24, ndalama zochokera ku mayiko ndi mabungwe otithandiza zikwera ndi 45.8 peresenti mchaka cha zachuma cha 2024/25.

### Momwe ndondomeko ya za chuma yakonzedwera (MK' ma miliyoni)

| Komwe boma lipeze ndalama | Ndondomeko Yachuma Ya 2023-24 (Yovomerezedwa) | Ndondomeko Yachuma Ya 2023-24 (Younikiridwa pakutha kwa chaka) | Ndondomeko Yachuma Ya 2024-25 (Yovomerezedwa) | Ndondomeko Yachuma ya 2024-25 |
|---|---|---|---|---|
| **Ndalama a zomwe boma lipeze** | **2,553,019** | **3,040,616** | **4,552,220** | **24.3%** |
| **Kuchokera mudziko mommuno** | **2,242,430** | **2,407,430** | **3,383,808** | **18.1%** |
| Misonkho | 2,128,090 | 2,198,090 | 3,257,273 | 17.4% |
| Ziphaso ndi zina | 114,340 | 209,340 | 126,535 | 0.7% |
| **Kuchokera kunja** | **310,589** | **633,186** | **1,168,412** | **6.2%** |
| Kuchokera ku may iko akunja | 12,433 | 18,445 | 72,693 | 0.4% |
| Kuchokera ku mabungwe akunja | 298,156 | 614,741 | 1,095,719 | 5.8% |
| **Ndalama zomwe zigwire ntchito** | **3,788,319** | **4,329,068** | **5,998,834** | **32.0%** |
| **Zoyendetsera ntchito za boma** | **2,957,289** | **3,251,193** | **4,227,175** | **22.6%** |
| Za ogwira ntchito m'boma | 926,982 | 1,021,842 | 1,121,981 | 6.0% |
| Malipiro a wogwira ntchito m'boma | 900,442 | 980,491 | 1,075,232 | 5.7% |
| Gawo loperekedwa ku peshoni | 26,540 | 41,351 | 46,749 | 0.2% |
| **Chiwongola dzanja ku Ngongole** | **914,864** | **931,480** | **1,455,690** | **7.8%** |
| Zolipira kungongole za kunja | 35,873 | 94,780 | 79,750 | 0.4% |
| Zolipira kungongole za mmonumo | 878,991 | 836,700 | 1,375,940 | 7.3% |
| **Zogwiritsa ntchito tsiku ndi tsiku** | **547,563** | **615,884** | **845,543** | **4.5%** |
| Ntchito zina ndi zina | 328,334 | 367,560 | 493,023 | 2.6% |
| Gawo la umoyo | 81,486 | 104,130 | 122,423 | 0.7% |
| Gawo la ulimi | 24,778 | 29,982 | 74,138 | 0.4% |
| Gawo la maphunziro | 52,513 | 52,416 | 73,060 | 0.4% |
| Kulipira zotsalira za zaka zam'mbuyo | 1,000 | 1,800 | 500 | 0.0% |
| Storage levy expenses | 5,800 | 5,992 | 7,303 | 0.0% |
| Zogulira chimanga | 12,000 | 12,000 | 22,000 | 0.1% |
| Za chisakho chapanayi | 41,652 | 42,004 | 53,097 | 0.3% |
| **Zopita ku mabungwe ena a boma** | **302,641** | **327,369** | **412,373** | **2.2%** |
| Road Fund Administration | 73,451 | 75,849 | 85,024 | 0.5% |
| Roads Authority | 5,000 | 5,000 | 6,200 | 0.0% |
| Malawi Revenue Authority | 62,755 | 64,830 | 97,653 | 0.5% |
| Subvented Organisations | 145,435 | 161,691 | 199,496 | 1.1% |
| Net Lending | 16,000 | 20,000 | 24,000 | 0.1% |
| **Zothandizira magulu ena a anthu** | **248,763** | **297,716** | **358,613** | **1.9%** |
| Zipangizo zotsika mtengo za ulimi | 109,817 | 109,817 | 161,285 | 0.9% |
| Gawo la boma la peshoni | 135,546 | 184,288 | 193,169 | 1.0% |
| Social Cash Transfer - Government | 2,800 | 3,010 | 4,159 | 0.0% |
| **Zina ndi zina** | **16,475** | **56,902** | **32,975** | **0.2%** |
| **Zachitukuko (mapulojeketi)** | **831,030** | **1,077,875** | **1,771,658** | **9.5%** |
| Chitukuko chogwiritsa ndalama zakunja | 600,280 | 797,077 | 1,387,058 | 7.4% |
| Chitukuko chogwiritsa ndalama zathu | 230,750 | 280,798 | 384,600 | 2.1% |
| **Kubwereka ndalama** | **1,235,300** | **1,288,452** | **1,446,614** | **7.7%** |
| Kuchokera kunja | 132,373 | 194,630 | 149,915 | 0.8% |
| Kuchokera mdziko mmomuno | 1,102,927 | 1,093,822 | 1,296,699 | 6.9% |

### CHINTHUNZI CHOYAMBA
### Ndalama Zotoleredwa 2024/25




**Mmene boma ligwiritsire ndalama**
Mchaka cha zachuma cha 2024/25, boma likuyembekezera kugwiritsa ndalama zokwana K5,998.8 biliyoni (yomwe ili 31.9 peresenti ya chuma chomwe dziko lino limapeza). Ndipo izi zikusonyeza kuti pali kukwera kwa 38.6 peresenti pa ndalama zomwe boma ligwiritse ntchito kulekana ndi K4,329.1 biliyoni yomwe idavomerezedwa mu ndondomeko ya zachuma ya mchaka cha 2023/24. Pa ndalama imeneyi, K4,227.2 biliyoni ipita ku malipiro a ogwira ntchito m'boma, chiwongola dzanja pa ndalama zomwe boma limangongola ku mabanki ndi mayiko ena, kugula katundu yemwe amagulitsidwa pa mtengo wotsikirako pofuna kuthandiza opeza mochepekedwa monga feteleza wa makuponi, komanso kuyendetsa ntchito za boma, pamene K1,771.7 biliyoni idzagwiritsidwa ntchito pa zitukuko za dziko. Ndalama ya chitukukoyi ndi 30 peresenti ya ndalama ya ndalama zomwe boma ligwiritse ntchito. Pa ndalama imeneyi, K384.6biliyoni idzachokera ku misonkho yomwe boma limatolera mdziko mommuno pamene mayiko ena atithandiza ndi ndalama yokwana K1,387.1 biliyoni. Ndalama yokwana K384.6biliyoni yomwe boma likuyembekezera kutolera mdziko mommuno yagawidwa pawiri: K289.6 biliyoni ipita ku likulu la boma pamene K95.0 biliyoni ipita ku makhonsolo.

**Kuperewera kwa ndalama yopita ku ndondomeko ya chuma**
Boma likuyembekezera kuti mchaka cha chuma cha 2024/25, ndalama zomwe layerekezera kuti ligwiritsa ntchito ziperewera ndi K1,446.6 biliyoni (yomwe ikuyimira 7.7 peresenti ya chuma chomwe dziko lino limapeza). Pali chilinganizo choti boma lidzabwereka ndalama ku mayiko akunja zokwana K149.9 biliyoni (zogwiritsa ntchito pa ntchito zachitukuko)) komanso ndalama zokwana K1,296.7 biliyoni zidzabwerekedwa mdzino mommuno.

### MMENE BOMA LAGAWIRA NDALAMA KU NTHAMBI ZAKE

**Ndalama za Malipiro za Anthu Ogwira Ntchito M' Boma**
Boma likuyembekezera kuti ligwiritsa ntchito ndalama zokwana K1,075.2 biliyoni popereka chipuputa misozi kwa ogwira ntchito mchaka cha chuma cha 2024/25, zomwe zikuyimira 9.7 peresenti kusiyana ndi K980.5 biliyoni yomwe idavomerezedwa mchaka cha zachuma cha 2023/24 Izi ndi kaamba koti boma lili ndi malingaliro wolemba aphunzitsi komanso ogwira ntchito muzipatala komanso lilemba ntchito anthu mu ma unduna wosiyanasiyana. Mmenemunso muli K70 biliyoni yokwezera malipiro a anthu ogwira ntchito m'boma.

**Ndalama Zomwe Boma Zogwirtsa Ntchito Tsiku ndi Tsiku**
Boma lili ndi chiyembekezo choti ligwiritsa ntchito ndalama zokwana K3,459.5 biliyoni, zomwe ndi zokwera ndi 38.8 peresenti kusiyana ndi zomwe zinavomerezedwa mchaka cha zachuma cha 2023/24. Ndipo ndalamazi zagawidwa motere: Kugula katundu ndi zina (K845.5 biliyoni); kubweza ngongole (K1,455.7 biliyoni); ndalama zopita ku nthambi zina zaboma (K412.4 biliyoni); zopita ku chisamaliro cha anthu (K358.6 biliyoni); komanso ndalama zogwira ntchito zina ndi zina (K32.98 biliyoni).


### MMENE NDALAMA ZAGAWIDWIRA MOGWIRIZANA NDI MFUNDO ZA CHITUKUKO ZA MALAWI 2063

Chomwe tajambula munsimu chikufotokoza momwe boma lagawira ndalama mogwirizana ndi ngodya za chitukuko komanso zothandizira kuti masomphenya omwe ali mu ndondomeko ya zachuma ya chaka cha 2024/25 atheke.

**Ngodya**
10.1 peresenti ya ndalama zomwe taziyerekezazi zipita ku ntchito zotukula ulimi, 1.9 peresenti ipita ku ntchito zotukula mizinda ya dziko lino ndipo 0.9 ipita ku ntchito za mafakitale.


**Zothandizira zake**
Boma layika padera 32.4 peresenti ya ndondomeko ya zachuma ku ntchito zophunzitsa anthu maluso omwe angathandizire potukula dziko lino. Ntchito zokonza mmene nthambi zaboma zikugwirira ntchito zawo zapatsidwa 43.4 peresenti, 0.4 peresenti yapita ku ntchito zotukula maluso pakati pa ogwira ntchito m'boma, ndipo 7.3 peresenti yapita ku ntchito zotukula chuma cha dziko.

### CHITHUNZI CHA CHIWIRI Kagawidwe ka ndalama zogwiritsa ntchito tsku ndi tsiku



| | |
|---|---|
| Zo lipilira zinthu zina | 1% |
| Za opuma pa ntchito | 6% |
| Chiwongola Dzanja | 42% |
| Zipangizo za Ulimi | 5% |
| Mabugwe ena aboma | 12% |
| Kugwiritsa ntchito katundu ndi maluso | 24% |
| Zoperekedwa kwa anthu | 10% |

### CHITHUNZI CHA CHITATU Kagawidwe ka ndalama ku gawo a ntchito za boma/selitala



| | |
|---|---|
| Ulimi, Chitukuko cha ulimi wothilira, chilengedwe ndi kusintha kwa nyengo | 10% |
| Kayendetsedwe ka Boma | 38% |
| Maphunziro ndi Chitukuko cha ntchito za manja | 16% |
| Kayendetsedwe ka boma ndi kutsatira malamulo | 10% |
| Umoyo ndi chiwerengero cha anthu | 12% |
| Mphamvu za magetsi, migodi, malonda ndi zokopa alendo | 1% |
| Malo, nyumba ndi chitukuko cha ku midzi | 6% |
| Mtengatenga ndi zipangizo zofalitsira uthenga za intaneti | 7% |

### GAWO LA NDALAMA KU ZIGAWO ZA MIP1 NDI ZOTHANDIZA (MK' ma miliyoni)

| Gawo | 2023-24 Yovomerezedwa | 2024-25 Yovomerezedwa | 2024-25 (%) |
|---|---|---|---|
| Ka chulukitsudwe ka za ulimi ngati malonda | 383,509 | 497,746 | 8.33% |
| Zipangizo za zachuma | 206,329 | 435,050 | 7.28% |
| Za kayendetsedwe ka boma ka bwino | 1,622,947 | 2,592,599 | 43,37% |
| Ka gwiridwe ka ntchito za boma koyenera | 234,532 | 262,327 | 4,39% |
| Kagwiritsidwe ntchito ka za chilengedwe kosamala | 63,660 | 21,206 | 0.35% |
| Kutukula luso la ogwira ntchito | 1,161,837 | 1,939,285 | 32.44% |
| Ntchito za ma Kampani | 33,233 | 64,570 | 1.08% |
| Kusintha kaganizidwe | 2,392 | 6,297 | 0.11% |
| Ntchito za makampani woti si a boma | 7,273 | 3,714 | 0.06% |
| Ku kweza mizinda | 72,606 | 155,527 | 2.60% |
| **Zonse pamodzi** | **3,788,319** | **5,978,322** | **100.00%** |

### NDALAMA ZOPITA KU NTHAMBI ZABOMA

Monga mmene mwaoneramu, 10 peresenti ya ndondomeko ya za chuma yapita ku ntchito za ulimi, chitukuko cha madzi, ndi kusintha kwa nyengo, 16 peresenti yapita ku maphunziro, 7 peresenti yapita ku ntchito za mtengatenga ndi mtokoma, 12 yapita ku ntchito za zaumoyo ndi chiwerengero cha anthu, ndipo ndalama zokwana 6 peresenti zapita ku chitukuko cha kumidzi.

## Ndondomeko yamagawo opindulila aMalawi

Izi ndi zina mwa ntchito zomwe zithandizire kuti aMalawi apindule ndi ndondomeko ya zachuma imeneyi

(MK biliyoni)

### NTHAMBI YA ULIMI, ULIMI WAMTHIRIRA, KOMANSO CHITUKUKO CHA MADZI


- **199.7B** yapita ku ntchito zogawa madzi ndi ukhondo
- **89.8B** ntchito za ulimi wothirira
- **161.3B** yapita ku ntchito yogula zipangizo za ulimi zotsika mtengo
- **22B** igwiritsidwa ntchito pogula chimanga chosunga mu nkhokwe za boma
- **43.5B** Kubwereranso kwa ADMARC kulimbikitsa zokolola ndi phindu
- **5.2B** yigwiritsidwa ntchito kupangira makina osiyanasiyana a zaulimi
- **14.2B** yigwira ntchito kuminda yikuluyikulu (megafarm)
- **30B** yapita ku NEEF kuti aMalawi apeze ngongole za ulimi

Chofuna kudziwa nchakuti zipangizo zaulimi zotsika mtengo, minda yikuluyikulu ija, ulimi wothilira komanso ngongole zaulimi zonsezi zulunjika ku ntchito yowonetsetsa kuti zakolola zikhale zochuluka kwambiri.

### NTCHITO ZAM-TENGATENGA NDI MTOKOMA

- **218.7B** igwira ntchito pokonza misewu
- **1.5B** igwira ntchito potukula ntchito za maulendo a pa pamadzi
- **3B** igwira ntchito zotukula maulendo a pa ndege
- **0.35B** igwira ntchito zotukula maulendo a sitima za pamtunda (njanji)

### ZA UMOYO



- **57.95B** igwira ntchito pogula mankhwala opita mzipatala zikuluzikulu
  - MK24.5B mzipatala zikuluzikulu
  - MK33.4B zipatala za m'maboma
- **7.05B** igwira ntchito zomanga zipata
- **1.08B** yapita ku chipatala cha khansa
- **17.2B** Kulimbikitsa zipatala kuti zipereke thandizo labwino
- **1.5B** igwira ntchito potumiza odwala ku mayiko

### NTCHITO ZOTUKULA MIYOYO YA ANTHU

- **4.1B** yapita ku ntchito za mtukula pakhomo
- **20.2B** yapita ku maphunziro a mkombaphala ndi chitukuko cha ana
- **9.97B** yapita ku MoGCDSW
- **0.45B** Albinism Action Plan & Disability Fund

Ndalama zolimbikitsa kuti a Malawi akagwire ntchito ku mayiko ena potero akatumize ndalama zakunja ku Malawi

### MAPHUNZIRO NDI NTCHITO ZALUSO

- **125.1B** yapita ku sukulu za ukachenjede (yunivesite) zaboma
- **128.8B** igwira ntchito yogulira zipangizo zophunzitsira ndi zophunzirira ku sukulu za pulayimale ndi sekondale
- **209B** Ministry of Education projects
- **24B** yapita ku thumba lomwe ophunzira a sukulu za ukachengede ochokera ku mabanja ovutika amakangongolako ndalama yolipirira fizi ndi zina



### CHITUKUKO CHAKUMUDZI



- **224.6B** yapita ku ntchito zomwe cholinga chake ndi kutukula madera akumidz
- **38.6B** yaperekeda ku thumba la chitukuko cha m'madera omwe akuyimiriridwa ndi aphungu a ku Nyumba ya Malamulo (CDF)
- **2.3B** yapita ku ntchito za chitukuko cha madzi, monga kukumba mijigo
- **6.2B** yapita ku thumba la chitukuko lomwe limapezeka pa khonsolo (DDF)
- **20.1B** igwira ntchito pomanga misewu ya mmizinda
- **14B** yapita ku ntchito yokonza zipatala za paboma